# LIU LA NAMIKANGO

Namikango Mission

**Volume 18(3), November 2018**


## Kumaliza Mu Buku la Luka Mutu 15

Chaka chino takhala ndi nthawi yophunzira Luka mutu 15. M' mutu umenewu Yesu akutiuza nkhani zitatu zimene zili ndi zotsatira zodabwitsa pa miyoyo yathu. Nkhani yoyamba ndi yokhudza nkhosa yosochera komanso m'busa wabwino amene akupita kukaiyang'ana. Mu Liu loyamba, tinaona zam'mene nkhani imeneyi ikugwirizirana ndi miyoyo yathu, komanso m'mene Mulungu amakhalira okonzeka ndi ofuna kupita kukayang'ana anthu amene ataika mchipululu cha moyo. Nkhani yachiwiri imene Yesu akufotokoza mu Luka mutu 15 ndi yokhudza ndalama yotaika komanso mzimayi wabwino amene akusiya ndi ntchito zouse yang'ana ndalamayo. Mu Liu lachiwiri, tinalingalira za uthenga wabwino wa nkhani imeneyi, yakuti ngakhale anthu amene ali wotaikira "mkati mwa nyumba" ya Mulungu sasiyidwa okha. Uthenga wabwino ndi wakuti Mulungu, chimodzimodzi mzimayi wabwinoyu, amafunafuna mkati mwa nyumba komanso kunja mchipululu, amakhala ofuna nthawi zonse kuyang'ana mpaka atapeza anthu otaika.

Mu Liu lachitatuli, tifotokoza za nkhani yachitatu imene Yesu akufotokoza mu Luka mutu15. Nkhani yachitatuyi ndi yodziwika bwino ndi ambiri a ife. Ndi nkhani ya ana wotaika, komanso atate wabwino amene akupita kukafuna onse awiri. Iyi ndi imodzi mwa nkhani za Yesu zodziwika bwino, ndipo ili ndi uthenga wabwino ochuluka oti itiuze, choncho tikhala ndi nthawi yowonjezera yakuti tiganizira za mau a Yesu. Nkhani yachitatuyi ili ngati kothera kwa chiphunzitso chimodzi. Pamene ili nkhani yabwino kwambiri, nkhani ziwiri zoyambirira zokhudza nkhosa yosochera komanso ndalama zatithandiza kutikonzekeretsa ku chiphunzitso chachikulu chimenechi. Sikuti zinangochitika mwangozi kuti Yesu akuyamba kufotokoza nkhani ziwirizi asanafotokoze nkhani yomalizira yaikuluyi. Nkhani ya nkhosa yotaika komanso ndalama yotaika zatipatsa njira zakuti tikuyenera kumvetsetsa zimene Yesu akufotokoza mu nkhani yaikulu yachitatu. Pamene mukuwerenga Liu lonseli, Ndikukulimbikitsani kuti mudzikumbukira nkhani zoyambirira ziwiri zija ndikuona m'mene zikugwirizirana ndi nkhani yaikulu yachitatuyi.

Monga mwa nthawi zonse, muli kulimbikitsidwa kuwerenga nkhani ya mwana wolowerera uja ndikuyesetsa kupeza malo anu mu nkhaniyo. Kodi ndi mwana uti mu nkhaniyi amene mukufanana naye? Nanga kodi uthenga wabwinowu ukumukhudza bwanji mwana ameneyu? Titakhala ndi nthawi yabwino ndi nkhani ya Yesu yachitatu tilingalira pa nkhani zonse zitatu pamodzi, kuona m'mene zonse zikulumikizirana. Ifeyo kuno ku Namikango timakonda Luka mutu 15 ndipo tikukhulupilira kuti ikupereka uthenga wabwino kwa wina aliyense. Tikupemphera kuti inunso mugwanso m'chikondi ndi mutu umenewu ndipo mutha kulandira uthenga wabwino umene Yesu akupereka.

-Eric Gephart

Pofuna kuti awerengi athu amvetse bwino phunziroli, tatenga mau ambiri mu Chichewa cha lero chopezeka mu Buku loyera *(Copyright 1988 by The Bible Society of Malawi).*

# Fanizo la Ana Wolowerera



Liwu lakuti kulowerera likutanthauza "kugwiritsa ntchito mosasamala." Timakonda kutchula fanizoli kuti ndi la mwana wolowerera, koma liwuli likufotokoza kwambiri za atate wake kuposa m'mene likufotokozera mwana. Atate ndiye phata mu nkhaniyi, amene Yesu akugwiritsa ntchito pakudzifotokoza yekha. Tikukumbukira kuti pali magulu awiri a anthu amene ali ndi Yesu pamene akufotokoza fanizoli. Pamene tikuwerenga, tikhoza kuyerekeza phwando mu nkhaniyi ndi ufumu wa Mulungu, mwana wang'ono ndi wokhometsa misonkho komanso anthu ochimwa, mwana wankulu ndi a Afarisi. Nkhaniyi ili ndi kumapeto kumene kukusowa pamene m'bale wankulu uja akusiyidwa kunja kwa phwando, kusiya anthu amene akuitsata nkhaniyi asakudziwa chenicheni chimene ati apange. Yesu akuwafunsa Afarisi, "Kodi mubwera ku phwando?" Nkhaniyi yalembedwera iwowo makamaka. Tiyeni tione nkhaniyi.

Nkhaniyi ikuyamba pakutiuza za atate ndi ana ake amuna awiri. Mwana wamng'ono akubwera kwa atate ake, ndipo akuwapempha bambo akewo gawo lake la chuma. Yesu wangonenapo mau ochepa, ndipo amene akumvetsera akuyenera kudzidzimutsidwa. "Bambo wa anawa alimoyo," Wina akhoza kunena kuti, "Mwanayu sakuyenera kupempha za gawo lake la chuma panopa!" Mu nthawi ya Yesu (zimenenso zimachitika kawirikawiri ku Malawi kuno), katundu sapita kwa ana pokhapokha makolo atamwalira. Malo sanali chinthu chimene munthu amakhala nacho. Chinali chinthu chimene nthawi zambiri chimakhala pa banja kwa zaka, choncho anali gawo la moyo wawo. Tikhoza kumvetsa thunthu la chinthu chimene mwanayu wopempha kuti zili ngati kuti: "Atate ndikanakonda mukanafa. Ndikufuna ndilandire zimene ndikuyenera kulandira panopa." Mwanayu sanangophwanya malamulo a chikhalidwe a m'mudzi mwawo, iye waswa mtima wa bambo ake ndipo wawauza bambo ake kuti awononge moyo wawo.

## Luka 15:11-24

Ndipo Iye anati, Munthu wina anali ndi ana amuna awiri; ndipo wamng'onoyo anati kwa atate wake, Atate, ndigawirenitu zanga za pa chuma chanu. Ndipo iye anawagawira za moyo wake. Ndipo pakupita masiku owerengeka mwana wamng'onoyo anasonkhanitsa zonse, napita ulendo wake kudziko lakutali; ndipo komweko anamwaza chuma chake ndi makhalidwe a chitayiko. Ndipo pamene anatha zake zonse panakhala njala yaikulu m'dziko muja, ndipo iye anayamba kusowa. Ndipo anamuka nadziphatikiza kwa mfumu imodzi ya dziko lija; ndipo uyu anamtumiza kubusa kwake kukaweta nkhumba. Ndipo analakalaka kukhutitsa mimba yake ndi makoko amene nkhumba zimadya, ndipo palibe munthu anamninkha kanthu.

Koma m'mene anakumbukira mumtima, anati, Antchito olipidwa ambiri a atate wanga ali nacho chakudya chochuluka, ndipo ine ndionongeke kuno ndi njala? Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga, ndipo ndidzanena naye, Atate, ndinachimwira Kumwamba ndi pamaso panu; sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu; mundiyese ine ngati mmodzi wa antchito anu.

Ndipo iye ananyamuka, nadza kwa atate wake. Koma pakudza iye kutali atate wake anamuona, nagwidwa chifundo, nathamanga, namkupatira pakhosi pake, nampsompsonetsa. Ndipo mwanayo anati kwa iye, Atate ndinachimwira Kumwamba ndi pamaso panu, sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu. Koma atateyo ananena kwa akapolo ake, Tulutsani msanga mwinjiro wokometsetsa, nimumveke; ndipo mpatseni mphete kudzanja lake ndi nsapato kumapazi ake; ndipo idzani naye mwanawang'ombe wonenepa, mumuphe, ndipo tidye, tisekere; chifukwa mwana wanga uyu anali wakufa, ndipo akhalanso wamoyo; anali wotayika, ndipo wapezedwa. Ndipo anayamba kusekera.

Koma chodabwitsa kwambiri kuposa pempho la mwanayu ndi yankho la atate…"ndipo iwo anawagawaniza chuma chake pakati pawo". Atatewo, amene tinakayembekezera kuti akwiya ndi kumutayira kunja mnyamatayu opanda kanthu, modzichepetsa anamugawira mnyamatayu zimene amafuna iye nkulolera kukhala ovutika

chifukwa cha mwana wake, ndi kupweteka kwa mumtima mwake. Ana onse awiri analandira zimene akanayenera kulandira Atate wawo atamwalira. Mwana wang'ono analandira gawo lake la chuma ndipo nsangansanga anagulitsa katunduyu kwa munthu, natenga ndalama, nauyamba ulendo kukapeza chisangalalo komanso ufulu kuchoka ku ulamuliro wa bambo ake. Mwana wankulu analandiranso gawo lake koma anakhala pakhomo pa makolo ake. Apa ndi zofunikira kuti tizindikire chinthu chinachake. Mu nkhani imeneyi, m'bale wankulu uja anayenera kukhala mkhala pakati wa pakati pa bambo ake komanso mng'ono wake. Iye anakana kuchita zimenezi. Choncho kuyambira pachiyambi, tikuona kuti mwana wankuluyunso sali paubale wabwino ndi bambo ake. Izi zikhala zofunika nthawi ina mu nkhaniyi.

Mwana wang'ono wapita ku dziko lakutali, wakakhazikika, ndipo tikuuzidwa kuti waononga gawo lake la chuma m'makhalidwe osakhala bwino. Patapita nthawi, kunakhala njala ndipo mwanayu alibe chilichonse, ndiye "wadziphatika" yekha ku mzika ya deralo. Iye wavutika kwambiri mpaka ali okonzeka kudya pamodzi ndi nkhumba. Ayuda amadana ndi nkhumba. Zikhoza kupangitsa munthu wa mtundu wa chi Yuda kukhala odetsedwa kudya nyama ya nkhumba, zimene zili zovutanso kuti adye zakudya zimene nkhumbazo zimadya. Zisankho za mwana ameneyu zamutsogolera ku malo ovuta kwambiri. Pa nthawi imeneyi, akuganiza zobwerera kwa atate ake, koma osati m'mene tingaganizire. Palibe umboni uliwonse wakuonetsa kukhudzidwa kapena kulapa kuchokera kwa iyeyu. Mwanayu akuyesera kulankhula zimene akawauze bambo ake: "Atate, ndinachimwira kumwamba ndinso pamaso panu…" Mau awa akumveka bwino, koma mau amenewa ndi mau enieni omwe Farao analankhula kwa Mose (Eksodo 10:16) pamene anavomera mwachinyengo kuti avomereze kuti Israyeli achoke ku Aigupto ngati Mose angamupemphe Mulungu kuti achotse mlili. Amenewa si mau owona enieni olapa.

Komanso, mwanayu akufuna kupita kwa bambo ake ngati "wantchito" mnyumba ya atate ake. Antchito amalipidwa. Akapolo salipidwa.

## Luka 15:25-32

Koma mwana wake wamkulu anali kumunda. Ndipo pakubwera iye ndi kuyandikira kunyumba, anamva kuimba ndi kuvina. Ndipo anaitana mmodzi wa anyamata, namfunsa, Zinthu izi nzotani? Ndipo uyu anati kwa iye, Mng'ono wako wafika; ndipo atate wako anapha mwanawang'ombe wonenepa, chifukwa anamlandira iye wamoyo. Koma anakwiya, ndipo sanafune kulowamo. Ndipo atate wake anatuluka namdandaulira.

Koma anayankha nati kwa atate wake, Onani, ine ndinakhala kapolo wani zaka zambiri zotere, ndipo sindinalakwira lamulo lanu nthawi iliyonse; ndipo simunandipatsa ine kamodzi konse mwanawambuzi, kuti ndisekere ndi abwenzi anga. Koma pamene anadza mwana wanu uyu, wakutha zamoyo zanu ndi akazi achiwerewere, munamphera iye mwana wang'ombe wonenepa. Koma iye ananene naye, Mwana wanga, iwe uli ndine nthawi zonse, ndipo zanga zonse zili zako. Koma kudayenera kuti tisangalale ndi kukondwerera: chifukwa mng'ono wako uyu anali wakufa ndipo ali ndi moyo; anatayika, ndipo wapezeka.

Iye sakufuna kubwerera ngati kapolo. Iye akufuna ndalama ndicholinga chakuti awalipire bambo ake, ndicholinga chakuti ulemu wake ubwerereranso m'mudzimo. Iye wadzipereka ku dongosolo limeneli ndipo wanyamuka kuti akayesere kuti bambo ake akamvetsetse zoti bambo akewo akamulole kubwereranso kunyumbako komanso m'mudzimo. N'chifukwa chake ngakhale atafika kumayambiriro kwa mudzi wawo anali wolowererabe.

M'chikhalidwe cha nthawi ya Yesu, munthu kudera akapanga zinthu zimene wapanga mwanayu (kuchititsa manyazi banja la kwawo komanso kuononga chuma ku dziko la anthu osaopa Mulungu) ndi kufuna kubwereranso kuderali, amayenera kudzera mu mwambo otchedwa Kezazah. Pamene akulowa muderali anthu a m'mudziwu amakhala pa nzere mphepete mwa nsewu wolowera m'mudziwo ndikumanyoza munthuyu (ndi kumamugenda ndi masamba) pamene akubwelera. Ndizochititsa manyazi kwambiri, koma munthuyu amayenera kubweza zonse zimene anazionga, apa ndi pamene amalandiridwa. Ndizosakaikitsa kuti mwanayu akuganiza zimenezi paulendo wake

wautaliwu kubwerera kwawo, pamenepa alipakati kuti akakumane ndi bambo ake ndi kukawauza zimenezi. Kwinaku, bambo ake akhala akudikirira pakhomo la nyumba yawo tsiku ndi tsiku, kuyang'ana ngati pangakhale chisonyezo chilichonse cha kubwera kwa mwana wake. Kenako, wamuona akubwera koma kutali, kachikenanso, tateyu akupanga zosaganizika; akumuthamangira kukakumana naye. Kodi ku Malawi kuno anthu akuluakulu a ulemu wawo amonetsa miyendo yawo ndi kuthamanga kwina kulikonse? Mu nthawi ya Yesu, amuna akuluakulu samathamanga! Zinali zinthu zochititsa manyazi kutero. Koma nanga n'chifukwa chiyani m'bambo uyu akuthamanga? Tikudziwa wasangalala kumuona mwana wake. Koma pali zinanso.

Bamboyu akudziwa zimene mwana wakeyu akuyenera kukumana nazo pamene akulowa m'mudziwu; mazunzo ndi manyazi amene akakumane nawo pamene anthu akapange mwambowo. *Choncho m'bambo ameneyu akuthamanga kudutsa m'mudzimu; kudzichititsa manyazi, cholinga zimenezi zisanchitikire mwanayu.* Akukumana naye m'malire mwa mudziwu. Ndi pamenepa pamene mwanayu akulapa *kwenikweni*. Ataona chionetsero cha chikondi cha mtengo wapatali kwa iyeyu kuchokera kwa bambo ake, iye asanalankhule liwu, malankhulidwe ake asintha; "Atate, Ndachimwa…sindili oyenera kutchedwa mwana wanu." Iye sakupitirizanso kupempha kuti akhale wantchito chifukwa pano akuona kuti bambo ake sangalole. Iye wakondedwa kwambiri. Sakuyeneranso kuchita kanthu kuti akondedwe; bamboyo waonetsera kale kuti kuyesera kulikonse kwa mwanayo kuti apeze chinachake kukhala kopanda ntchito. Atate wake akumukonda kale komanso akumulandira. Akulandira mphete, mkanjo, ndi nsapato; zizindikiro zimene zikuti, "Uyu ndi mwana wanga wokondedwa wa banja langa, osati wantchito." Tsopano mwanayu adzipatsidwa ulemu chimodzimodzi ngati m'mene bambo ake alili.

Choncho mu chithunzithunzi chodabwitsa, Yesu waonetsa kwa anthu amene akumva mau ake zam'mene Mulungu akuwalandirira okhometsa misonkho komanso ochimwa; mogwirizana ndi nkhosa yosochera komanso ndalama yotaika kumene wina akuyenera kupita kukabwezeretsanso otaika, apa tili ndi atate amene akuchoka kunyumba kwake ndi kupita kunja kukavutika ndi kubwezeretsa mwana wake wolowerera. Kodi ichi si chinthu chimene Yesu wachita kusiya nyumba yake ya kumwamba kubwera kudzafunafuna ndi kupulumutsa inu ndi ine, ndi kudzavutika chifukwa cha ife? Uthenga wabwino, umene tikuona, ndi wakuti ife tonse tisakhale oyenera kapena kugwirira ntchito, kuti uzipulumutse, Mulungu amatikonda tonse ndipo anabwera kudzatipulumutsa ife. Ichi ndi chithunzithunzi cha mphamvu chimene Yesu akutipatsa, ndipo tili ndi atate wa mphamvu. Uwutu ndi uthengandi wabwino!

Apa, nthawi zambiri mpamene timasiira nkhaniyi, kukhazikika pa phunziro lalikulu limeneli kuchokera ku fanizoli, ngati kuti limeneli ndi phunziro loyamba limene Yesu akuphunzitsa. Ndilalikuludi, koma ngati limeneli ndiye phunziro loyambirira, nkhaniyi siikanapitirira. Ikanathera pomwepo. Koma nkhaniyi siikuthera pomwepo. Tiyeni tsopano tipitirize….

Tsopano atate akupanga phwando kunyumba kwake kumene waitana anzake kudzasangalala pakuchita bwino kwake pakubwezeretsa mwana wake wolowerera. Komabe, mwana wankulu (liwu limene lagwiritsidwa ntchito apa ndi "wankulu liwu limene limagwiritsidwa ntchito kufotokoza Afarisi; palibenso funso lakuti mwanayu akuimilira ndani") uja ali kubusa, ndiye pamene akuyandikira kunyumbaku akumva kuchokera kwa ka mnyamata koyandikana nako kuti m'bale wake wabwera, ndipo bambo ake ayanjana naye. Kuli kwina, ndiye kuti, pakhoza kukhala kukumana pamene mwanayu wabwera pa zam'mene kubwera kwake kungaonedwere. Mwanayu akudziwa kuchokera ku mau ochepawa kuti sipakhalanso kukambirirana. "Mwanayu walandiridwa."

Mwana wankulu wakwiya, ndipo akukana kukakhala nawo pa phwandoli ndi chisangalalochi. Pamenepanso, tikuyenera kumvetsetsa kuti kukana kulowa kumeneku ndi mwano waukulu kwa atate chimodzimodzi umene mwana wang'ono uja

Volume 18(3), November 2018

anapanga. Mwana wankuluyu anayenera kutumikira alendo amene anabwera pa phwandoli. Koma m'malo mwake akunyozetsa bambo ake, ndipo aliyense amene ali pa phwandoli akudziwa. Tate wabwino bwino akuyenera kumukana mwana ameneyu kuti siwake. Koma uyu si tate wabwino bwino. Iyeyu pamenepa akuchitanso zosaganizirika. Akupitanso panja (liwu mu mawu ndi "kuyanjanitsa") pakuyang'ana mwana wina, bamboyu kudzinyozetsa chifukwa cha chikondi pa mwana ameneyu. Ana onse ndi okondedwa ndi bambo wawoyo. Iye akuvutika modzipereka chifukwa cha onse awiri.

Pamene bambo usa wamufikira mwanayu akunyozedwanso kwambiri, pamene mwanayu akuti, "Taonani! Ine ndakhala kapolo ndipo sindinalandire kanthu." Chinthu choterechi sichinganenedwe kwa munthu wankulu, komanso makamaka bambo ako. Mtima wa mwanayu tsopano waululika. Iye akudzikhulupilira kuti ndi kapolo, ndipo amangofuna zinthu basi kuchokera kwa bambo akewa. Iye akupitiriza kunena kuti "mwana wanuyu;" sakutha mkumutchula mkomwe kuti m'bale wake. Mwanayutu ndi wotaikadi, ali kutali ndi atate ake, komanso banja la kwawo. Iyenso sikuti wangophwanya miyambo, komanso mtima wa bambo wake. Koma atatewa *kachikena akumuyankha mwachikondi chodabwitsa komanso modekha,* m'mawu wodabwitsa awa: "Mwana wanga, iwe uli ndine nthawi zonse, ndipo zanga zonse zili zako…" Liwu limene lagwiritsidwa ntchito lakuti "mwana" pamenepa si liwu wamba pa mwana: likutanthauza "mwana wanga wokondedwa." Atate akuuza mwanayu kuti iye wakhala ali mwana nthawi yonse ngakhale samazindikira zimenezi. Iye samafunikiranso kuchita zinthu mwa ukapolo chifukwa cha chinachake; chuma chonse, chisangalalo ndi mtendere za atatewa zinali zake chikhalire.

Nkhaniyi ikuthera pamenepa. Mau a mtengo wapataliwa ndi amene Afarisi akumva kuchokera kwa Yesu. Iwowo eni, amene amakhulupilira kuti ndi olungama, akuuzidwa kuti ndi wotaika. Iwo ali kunja kwa phwando. Ndipo awa "abale ang'ono" alimkati. Kodi izi ndi zotheka bwanji? Monga atate aja, Yesu akuwadandaulira mong ana ake okondedwa, kuti asiye chilungamo cha iwo eni ndi kukakhala nawo mu chikondwerero chimene Mulungu akuchita.

Pamene nkhani sinamalizidwe, kapena yatha ndi funso mu Baibulo, zikutanthauza kuti nkhaniyo ikupita kwa ifeyo. "Kodi inu mudzapanga chiyani?" Tikuona kuti mfundo ya nkhani ya Yesu siikupita kwenikweni kwa iwo amene ali "ochimwa" amene anachita chilichonse cholakwika, koma kwa a Khristu amene ali ndi chilungamo cha iwo eni amene amachita chilichonse chimene Baibulo limanena. Chokhudza kwambiri cha nkhaniyi sikuphwanya malamulo kapena kusunga malamulo, koma kuphwanya ubale ndi atate. Ndizotheka kusunga malamulo onse, Yesu akutero, koma mkukhala kutali kwambiri ndi atate. Ndizothekanso kuphwanyanso malamulo ndikukhalanso kutali ndi atate. Koma Yesu akuitana onse kuti awone kutaika kwawo, kuti adziwe kuti ndi wokondedwa, ndi kukhala osinthika.

-Ben Hayes

# Zowerenga Zina

Takambiranano nkhani zonse zitatu zimene Yesu akufotokoza mu Luka mutu 15. Zimene tapeza ndi zakuti nkhani zonse zitatu zikufotokoza chinthu chimodzi. Tiyeni tione m'mene nkhani iliyonse ikugwirizirana ndi zinazo.

Taona kuti mu nkhani ya nkhosa yotaika, nkhosayi ikusiya m'busayo ndi kukasochera mchipululu. Nkhosayo yataika ndipo siingathenso kubwerera kwawo ndipo ikuyenera kudalira m'busa wabwino kubwera ndi kudzaipeza. Chinthu chomwechonso chikuchitika mu nkhani ya ana awiri olowerera. M'bale wang'ono akusiya nyumba ya atate ake ndipo akukasochera ku chipululu, kutali kumizinda ya anthu osaopa Mulungu. Iye wasochera kwambiri oti sangathenso kukhala ndi chiyembekezo chopezeka mpaka atate wabwino atathamangira kumsewu ndi kukamupulumutsa. Monga tinafotokozera poyamba, nkhosa yotaika komanso m'bale wang'ono wotaika akuimilira anthu ochimwa ndi

okhometsa misonkho amene anali mchigulu cha anthu kumvera nkhani zimenezi mu Luka mutu 15:1. Anthu awa ndi otaika ndipo akuyenera kudalira pa m'busa wabwino, atate wabwino, kuti abwere mchipululu mwawo ndi kuwapeza!

Lingalirani pa nkhani ya nkhosa yotaika komanso mwana wang'ono wotaika. Kodi inu munayamba mwakhala ngati nkhosa yotaika? Kodi munayamba mwakhala ngati mwataika mchipululu? Kodi mukumva Yesu akukulankhulani chiyani mu nkhani zimenezi?

Chimodzimodzi, tinaona mu nkhani ya ndalama yotaika imene inagwetsedwa ndi kusowa mnyumba ya mzimayi. Ndalamayi siinataike kuchipululu monga nkhosa ija, mmalo mwake, yasowera pamapazi amzimayiyu. Ngakhale zili chonchi, ndalamayi ikufunika thandizo kuti ipezeke ndipo ikuyenera kudalira mzimayi wabwinoyu kuyang'ana mnyumba yake mpaka aipeze ndalama yotaikayi. Ndalama yotaikayi ili ngati m'bale wankulu wotaika uja. Iye wataika mnyumba ya atate wake, osati kunja ku chipululu monga m'bale wang'ono uja. M'bale wotaika wankulu uja ali pafupi ndi atate ake, koma iyenso ndi wotaikanso chimodzimodzi. Monga ndalama yotaika ija, mwana wankulu wotaikayu akuyenera kudikilira mzimayi wabwinoyu, atate wabwino, kuti amuyang'ane mnyumbamo kuti amupeze. Monga tafotokoza kale poyamba paja, ndalama yotaikayi komanso m'bale wankulu wotaikayu akuimilira a Afarisi ndi aphunzitsi a chilamulo amene ali mu gulu la anthu kumvera nkhani zimenezi mu Luka 15:1. Anthu amenewa akuganiza kuti ndi opembedza kwambiri chifukwa amamvera chilamulo cha Mulungu, koma ndi wotaika chimodzimodzi ochimwa aja komanso okhometsa misonkho. Iwo onse akufunika atate wabwino kuti abwere adzawapulumutse!

Lingalirani pa nkhani ya ndalama yotaika komanso m'bale wankulu otaika uja. Kodi munayamba mwakhala ngati ndalama yotaika? Kodi munayamba mwakhala ngati mwataika ngakhale munali chifupi ndi Mulungu? Kodi mukumva chiyani kuchokera kwa Yesu mu nkhani zimenezi?

Tikuonanso kufanana kwina mu nkhani zitatu zimenezi. Pamene m'busa wabwino wapeza nkhosa yake yotaika, akupita nayo kunyumba, akuitana anzake pamodzi, ndipo akupanga phwando. Chimodzimodzinso pamene mzimayi wabwinoyu wapeza ndalama yake, akuitana anzake kuti abwere kunyumba ndipo akupanga phwando. Mzimayi wabwinoyu ndi osangalala kwambiri kuti wapeza ndalama yake ndipo akusangalala ndi anzake. Nanga atate wabwino uja akupanga chiyani pamene mwana wake wang'ono uja wapezeka komanso wabwerera kunyumba? Iye akuitana anzake pamodzi ndipo akupanga phwando! Atate wabwinoyu ali osangalala kwambiri kuti mwana wake wapezeka ndipo akuyenera kusangalala ndi anzake. Momwemonso, Yesu akutiuza kuti Mulungu amasangalala kwambiri pamene wapeza mwana wake wotaika ndipo amawapangira phwando. Mulungu sakwiya kapena kukhumudwa nafe akatipeza, iye amakhala osangalala kwambiri moti amakonza phwando kusangalala!

Ngakhale kuti Yesu akumaliza nkhani yake yachitatu tisanaone kuti chachitika ndi chiyani ndi m'bale wankulu wotaika uja, tikhoza kungoganizira zinthu zingapo kuti zinachitika ndi iye. Chinthu choyamba chimene tingaganizire, ndi chakuti m'bale wankuluyu anaganiza zobwereranso kunyumba ya atate ake, atate akasangalala kwambiri moti akapitiriza kusangalala, mwinanso kukonza chakudya china kuonjezera kuti alendo aja adye. Komabe, ngati mwana wankuluyu ataganiza zoti akhalebe wotaika kunja kwa nyumba ya atate wake, tikhonzanso kuganiza kuti atate ake samusiya koma apitirize kumusaka mwana wake wotaikayu ndi kumubweretsa kunyumba ya atate ake. Mulungu ndi Mulungu amene amasaka. Iye amakonda kupita kunja kukasaka anthu amene ataika, kaya ataika mchipululu, kapenanso ngakhale atataika mnyumba.

Kodi Yesu akutiuza nkhani yabwino yotani mu nkhani zitatuzi zimenezi?

Kodi tikuphunzira chiyani chokhudza anthu mu nkhani zitatu zimenezi?

Kodi tikuphunzira chiyani chokhudza Mulungu mu nkhani zitatu zimenezi?

Kodi nkhani zitatu zimenezi mungazigwiritse bwanji ntchito m'moyo wanu?

-Eric Gephart